# KULOWETSAKO CHUMA

. . .kudzakhala ndi maminiti pang'ono awa ndi anthu inu. Ndipo ndine woyamikira kwa M'bale Pearry chifukwa cha kundiyitana uku kuti ndidzakhale kuno, ndi chifukwa cha mgwirizano wanu wonse.

2 Ine ndikuganiza uku ndi kudzacheza kwathu kwachitatu ku mzinda wanu wabwinowu. Ife nthawizonse takhala tikuwapeza anthu kuno amsangala, ndipo nthawizonse amayankhula, amapereka, kaya iwo akukudziwa iwe, kapena ayi. Ine ndimayendera malo ena amalonda, ndipo ndizabwino bwanji. Nthawizonse zimawoneka zosiyana kuposa momwe izo zimakhalira kumpoto kozizira; iwo amandiwona ine ndikulowa mkati, iwo amadikirira pa iwe ndi kudzatuluka kunja, ndipo ndizo zonse za zimenezo. Koma iwe sumabweranso pamalo kupatula ngati wina akuyamikira iwe ndikuti, "Zikomo inu! Mudzabwerenso ndi kudzatiwona ife kachiwiri!" Ine ndimazikonda zimenezo.

3 Ndiye, ine ndikuganiza kuti M'bale Pearry apa, monga ine ndikanamutchulira iye izo, basi. . .Ndine wamkulu kuposa abambo ake, chotero ine ndikuganiza ine ndikhoza kumutcha iye M'bale Pearry. Ife sitimamudziwa nkomwe mnyamatayo, tinamudziwa mwana wanga, Billy Paul atatidziwitsa ife, ankapita limodzi ku sukulu ndi iye. Koma ngati alipo aliyense mu mzinda uno, kapena kozungulira, mwa kufikira kwa televizioni, yemwe ati adzataike pa tsiku lotsiriza, izo sizidzakhala chifukwa chakuti M'bale Pearry sanaike kuyesetsa kulikonse kuti ayesere kuwatengera anthu kwa Khristu. Iye ndithudi sanasiye mwala umodzi wosagudubuzika. Ndipo ine ndikuwutenga uwu mwayi wopambana wa kudzakhala pano.

4 Pamene M'bale Pearry anandipempha ine, ngati ndingati "ndidzayankhule pa phwando laling'ono" limene iye anali nalo, kuti ena a azimzake amalonda akanadzakhala ali kuno. Chabwino, ndine ndithudi osati woyankhula. Ine—ine sindimadzinenera kuti ndine chimenecho, koma ndinaganiza kuti ndikanadzatero. Ungakhale ulemu kwa ine, nditakhala ndi kuyitana konga kumeneko, kuti ndidzayankhule kwa—ndi. . . azimzake amalonda.

5 Ine ndakhala nawo mwayi woyenda konsekonse, kuzungulira dziko lapansi. Ndipo ine ndimawayankhulira mochuluka a Full Gospel Business Men. Ndipo ine ndikudziwa kuti iyi ndi nthawi yaing'ono chabe ya chiyanjano, chotero ine ndikufuna kuti ndifotokoze chinachake chimene chinali chokongola nthawi ina. Panali munthu, ine nditatsiriza kuyankhula. . .Iwo onse anali amuna amalonda. Ndipo, chotero,

kunja uko kunali munthu amene anabwera kwa ine, ndipo iye anati, “Ndinu mlaliki, si choncho inu?”

Ndipo ine ndinati, “Inde, bwana.”

6 Iye anati, “Kodi ndi chifukwa chiyani mumangolondana nawo amuna amalonda awa?”

Ine ndinati, “Ndine munthu wamalonda.”

Kotero iye anati, “Oh, inu muli?”

Ndipo ine ndinati, “Inde, ndine—ndine munthu wamalonda.”

Anati, “Kodi ndi inu mukuchita bizinesi ya mtundu wanji, bwana?”

Ndipo ine ndinati, “Chitsimikizo cha Moyo Wamuyaya.”

7 Ndipo iye sanandimvetse ine molondola basi. Ine ndinanena izo mofulumira. Iye anati, “Oh, a—Inshuranse ya Moyo Wamuyaya.” Ine sindinati inshuranse; ine ndinati chitsimikizo, ndipo iye. . .Koma ine sindinamuuze konse iye. Ndipo iye anati, “Moyo Wamuyaya,” anati, “Ine sindikuzidziwa. Ine sindikukhulupirira kuti ndinayamba ndamvapo za izo kale.”

Ine ndinati, “Izo ndi zoipa kwambiri.”

Anati, “Chabwino,” iye anati, “likulu lake liri kuti?”

Ine ndinati, “Kumwamba.”

8 Ine ndikadali mu bizinesi imeneyo. Ine ndikufuna kuti ndiyankhule za ndondomeko yake ndi aliyense wa inu, msonkhano ukatha, usikuuno. Ine ndatengeka kwambiri ndi ntchito yanga. Ndipo, chotero, ndipo ine sindinati konse tsopano, “inshuranse,” ine ndinati, “chitsimikizo.”

9 Inshurance ndi yabwino, ndikumvetsedwa. Ine ndikumbukira. . .Ndithudi, ine pa nthawi ino ndiribe iliyonse.

10 Ine ndikukumbukira, nditamukwatira, mkazi wanga ndipo ndinali nditakhala mnyumba, tsiku lina. Ndipo mzanga wabwino wa ine. . .M’bale wanga amagulitsa inshuranse, Kummwera-Chakumadzulo. Mnyamata uyu anali wogulitsa Prudential. Ine ndinkapita ku sukulu naye iye, mnyamata wabwino kwambiri. M’bale wake—wake amalemba *The Upper Room,* pakuti, ine ndikukhulupirira iye ndi mtumiki wa Baptisti, ndipo iye amalemba nkhani mu pepala yaing’ono yotchedwa *The Upper Room.* Anthu abwino kwambiri. Chotero iye anabwera kuti adzandiwone ine, tsiku lina, ndipo iye anati, iye anati, “Billy, ine—ine ndikumva kuti iwe unali ndi kobaya kakang’ono nthawi ina pa inshuranse.”

Ndipo ine ndinati, “Inde.”

11 Iye anati, “Izo zikukhala ngati zinakupatsa iwe kumverera konyungunya pang’ono kwa iwo?”

Ine ndinati, “Ayi, osati kwenikweni.”

Iye anati, “Ine ndimaganiza kuti ndibwere ndi kudzayankhula nawe za ndondomeko yake, Billy.”

12 Ndipo ine ndinati, “Chabwino,” ine ndinati, “Wilmer, zikomo,” ine ndinati, “koma ine—ine ndiri nacho chitsimikizo.”

Ndipo iye anati, “Oh, ine ndikupepesa.”

13 Ndipo mkazi wanga anayang’ana pozungulira ine, ngati kuti ine ndinali wachinyengo. Iye ankadziwa kuti ine ndinalibe iliyonse. Iye anayang’ana pa ine basi modabwa. Ine ndinati . . .

14 “Oh,” iye anati, “Ine ndikupepesa, Billy.” Iye ayenera kuti amaganiza kuti ine ndinali nayo iyo ndi m’bale wanga, Jese. Ndipo ine ndinati . . .

Mkazi wanga anandiyang’ana ine. Ndipo iye . . . Ine ndinati, “Inde, ine ndiri nacho chitsimikizo.”

Ndipo iye anati, “Ukuchita ndi kampani yanji?”

Ndipo ine ndinamuuza iye chinthu chomwecho, “Moyo Wamuyaya.”

Ndipo iye anati, “Oh,” anati, “kodi ndi imeneyo?”

15 Ndipo ine ndinati, “Eya. Ine ndiri nayo: Chitsimikizo chodala, Yesu ndi wanga! Oh, kulawiratu kwake kwa ulemelero Wauzimu! Ndine wolandira wa chipulumutso, wogulidwa ndi Mulungu, Wobadwa ndi Mzimu Wake, wotsukidwa mu Magazi Ake.

16 Iye anati, “Billy, izo nzabwino kwambiri. Ine ndikuyamikira zimenezo. Koma zimenezo sizidzakuika iwe kuno mmanda.”

17 “Koma,” ine ndinati, “izo zizanditulutsamo ine. Ine sindikudandaula . . . ” Uh-huh. Eya. Ine sindikudandaula za kulowamo; ndi za kutulukamo.

18 Ine ndikufunabe kuyankhula za ndondomeko yake kwa iwe, ukatha msonkhano, ngati . . . ine ndikutsimikiza Izo nzoona.

19 Tsopano, ine kawirikawiri ndimawapanga anthu kuti aime pamene ife tikuwerenga Mawu, koma, usikuuno, ine ndiyesetsa kuzilumpha izo chifukwa izo ziri—zikhala zovuta kwambiri kuti inu muyimirire. Koma basi ife tisanawerenge Mawu, tiyeni tingoweramitsa mitu yathu kwa mphindi pang’ono, pamene ife tikuyankhula kwa Mlembi wa Mawu. Monga ife takhala ngati tikuseka wina ndi mzake, ndi kukhala ngati tikutsika, kapena, monga momwe timadzitchulira izo, “kulekerera tsitsi lathu.” Chotero tiyeni ife tifike ku mbali yopatulika tsopano, ndi kuwona mtima, ndi kutembenuzira mitima yathu cha Kumwamba pamene ife tikutsegula Mawu. Tsopano munthu aliyense amene angathe kusuntha manja ake akhoza kutsegula Baibulo, koma palibe aliyense angakhoze kwenikweni kutsegula kumvetsa koma Mzimu Woyera waukulu, chotero tiyeni ife tiyankhule kwa Iye.

20 Atate athu Akumwamba, ife ndithudi takondweretsedwa, usikuuno, kuti tasonkhana pano ndi gulu ili la anthu, mbali iyi ya Muyaya, ndi kukhala ndi chiyanjano chabwino ichi. Ndipo pamene ife takhala kuzungulira magome awa, usikuuno, tikuyang'anizana wina ndi mzake, ndi abwenzi amalonda ndi—ndi Akhristu, ife tikuzindikira kuti kukubwera nthawi ina imene ife titi tidzakumane. Ife tikudalira kuti ife tonse tidzakakhala Kumeneko, aliyense amene alipo pa Mgonero wawukulu wa chikwati uwo mu mlengalenga, pamene Mfumu idzatulukire, kudzapukuta misonzi yonse kuyichotsa mmaso mwathu, ndi kuti, "Izo mwachita bwino, antchito Anga abwino ndi okhulupirika, lowani mu zisangalalo za Ambuye, zimene zinakonzeredwera inu chikhadzikitsireni maziko a dziko lapansi."

21 Ngati pangakhale ena, Ambuye, amene sakukudziwani Inu mwanjira imeneyo, ndipo ine ndikupemphera usikuuno kuti chinachake chichitike kapena kunenedwa kuti chiwapangitse iwo kuti asinthe njira yawo ya kaganizidwe, atembenukire kwa Inu; kaya iwo ali pano, kapena mwa—njira ya televizioni, kapena mwa matepi amene akhale akutuluka kuchokera pa izi.

22 Tidalitseni ife limodzi tsopano, ndipo mudalitse kuwerenga kwa Mawu Anu. Tembenuzirani mitima yathu ndi maganizo cha ku mathero a moyo uno, ndi chomwe chidzakhale chikhalidwe chathu pa nthawi imeneyo. Pakuti ife tiri otsimikiza, Atate, kuti tonse a ife tiyenera kuti tidzalisiye dziko lino. Ndife achivundi, ndipo mutilole ife tiyang'ane kwa Iye Wamuyaya, Mmodzi yekhayo amene angatipatse ife Moyo kuseri kwa izi. Kupyolera mu Dzina la Mwana Wake, Yesu Khristu, ife tikupempha izi. Ameni.

23 Ine ndikufuna kuti ndiyitanire tcheru chanu, kwa mphindi pang'ono tsopano, ku kuwerenga kwa Mawu a Mulungu. Ine ndikufuna kuti ndiyambe kuwerenga kuchokera ku Uthenga wa Marko Woyera, ine ndikuganiza mutu wa 10, ndipo kuyambira ndi ndime ya 17.

> *Ndipo pamene iye anali atapita mu njira, apo panabwera* kwa iye *wina akuthamanga, ndipo* anagwada pansi*. . . ndi* kumufunsa *iye,* akuti, *Mphunzitsi Wabwino, kodi ine ndichite chiyani kuti ine ndikhoze kulandira moyo wamuyaya?*
>
> *. . . Yesu anati kwa iye, "Chifukwa chiyani iwe ukunditcha ine wabwino? palibe wina wabwino koma mmodzi,* ndipo *ameneyo ndi, Mulungu.*
>
> *Inu mukuwadziwa malamulo, Musati muzichita chigololo, Musati muphe, Musati muziba, Usachite umboni wonama, Usanyenge, Lemekeza atate ako ndi amako.*

> *Ndipo iye anayankha nati kwa iye, Mphunzitsi,* zinthu *zonse izi* ine *ndazichita* kuyambira *unyamata wanga.*
>
> *Ndiye Yesu atamuyang'ana iye anamukonda iye, ndipo anati kwa iye, Chinthu chimodzi chimene iwe ukuchisowa: pita panjira yako, ukagulitse chirichonse chimene iwe uli nacho, ndipo ukapereke kwa osauka, ndipo iwe udzakhala nacho* chuma *kumwamba: ndipo ubwere,* ndipo *udzatenge mtanda* wako, *ndipo udzanditsate ine.*
>
> *Ndipo iye anali wachisoni pa kunena kumeneko, ndipo anachokako atakwiyitsidwa: pakuti iye anali ndi chuma chochuluka.*

24 Ambuye awonjezere madalitso Ake ku Mawu pamene ife tikuyesera kuti tikoke kuchokera mu awa mutu ndi nkhani. Tsopano kuganiza pa phunzirolo la kukhala ndi anthu amalonda, ndipo nthawizonse ine ndikuganiza kuti anthu amalonda nthawizonse amakhala ndi chidwi mu—mu kulowetsako chuma kwabwino, kotero kuti nditengeko phunziro tsopano kwa mphindi zingapo zotsatirazi: *Kulowetsako Chuma.*

25 Wamalonda wabwino nthawi zonse amafuna a—kwabwino, kulowetsako chuma kokhazikika. Ngati iye sangatero, ndiye iye si wamalonda wabwino. Iye amayenera kuyang'ana chinachake chimene chiri chenicheni.

26 Ndipo ine ndikufuna kuti ndiyankhule nanu pa kuitanidwa kumene ine ndapereka kwa inu mphindi pang'ono zapitazo, pa ndondomeko iyi ya Moyo Wamuyaya, monga ine ndinadziwonetsera ndekha ngati a—munthu wamalonda. Ndipo ine ndiri nayo bizinezi, ndipo ine ndikufuna kuti ndiyankhule kwa inu mphindi pang'ono za iyo. Ndi Malemba pang'ono amene ine ndawalemba apa, ndi mutu, ine ndikufuna kuti ndizigwiritse ntchito izi kwa mphindi pang'ono, zolemba izi.

27 Si a—malonda abwino kuchita njuga. Munthu aliyense amadziwa zimenezo, kuti njuga si malonda abwino, chifukwa iyo ndikutengerapo mwayi. Inu simungati, kapena si kawirikawiri mungamuwone wochita njuga. . .Tsiku lina iye amakhala munthu wolemera, ndipo tsiku lotsatira iye akupemphetsa. Kotero imakhala ngozi kwambiri, kuti—uzichita njuga. Ine ndikuganiza a—a—wochita njuga ndi—basi amangokhala moyo wosakonzekera za mtsogolo la nthawi, ndipo samayang'ana ndi chiyembekezo za zam'tsogolo, kapena iye sibwenzi akuchita njuga.

28 Ndipo ine sindimakhulupirira zina zazinthu izi za kulowetsako chuma kuti ulemere mu-usiku-umodzi, nkomwe, za malonda ena osadziwikawa. Tsopano, wamalonda wabwino aliyense sangatengerepo mwayi monga chomwecho, mwinamwake pa zanu—zosunga zanu za pa moyo, zimene mwazipeza; ndipo nkukazilowetsa izo mu zosachedwa-kupeza,

kulemera-kwamsanga. Ndipo ndi zosadziwika. Winawake kuthamangira mmenemo ndi mtundu winawake wa lingaliro, kuti, "Kuno ife—ife tiri ndi kampani inayake kuno," yopanda maziko a zimenezo. Ine ndikuganiza kuti munthu wabwino, woganiza bwino angakhale wopusa kuyesera kuyikako chuma mu yoteroyo a—kampani ngati imeneyo.

29 Chifukwa, ine ndinali ndi mzanga, nthawi ina, amene—amene anayeserapo chinthu choterocho. Ndipo, pamene iye anatero, iye—iye anataya chirichonse chimene iye anali nacho, ndipo iye anataya ndalama zonse za pa moyo wake. Ali pafupifupi kukonzekera kuti apume, ndipo iye anaganiza, "Chabwino, ine ndi—ine nditenga mwayi uwu," chifukwa munthuyo ankawoneka kuti amadziwa zimene iye anali kuzikamba. Koma, anadzapeza kuti, a—kampaniyo inangokhala kampani yodzipangitsa-kukhulupirira, ndipo inalibe masheya kapena kalikonse, kotero munthu wosaukayo anataya chirichonse chimene iye anali nacho.

30 Chotero ine ndikuganiza, ngati munthu akufuna kuyikako chuma, poyamba iye aziyifufuza kampani yakeyo, kapena chirichonse chimene iye akufuna kuyikamo chuma chakecho, ndi kufufuza zimene iye ati adzachite. Ine ndikuganiza munthu woganiza bwino aliyense angachite zimenezo.

31 Ndiyeno kachiwiri, ine ndisanapitirire, ine ndikufuna kunena kuti, ilo si lingaliro labwino kusunga ndalama zanu mthumba mwanu. Anthu ambiri amati, "Ine ndi—ine ndingoyika izo mthumba mwanga, ndipo ine—ine . . . ndipo ndikhala ndiri nazo izo." Koma, inu mukudziwa, inu amuna amalonda ndi akazi, inu musamaganize mwanjira imeneyo. Ndipo icho si chinthu chabwino, chifukwa izo zikhoza kubedwa.

32 Ndi chabwino kukhala nazo izo kuti zizungulira. Monga Ambuye ananena, nthawi ina, Iye anapereka matalente ochuluka kwa ambiri, ndi ena otero, ndiyeno iye . . . iwo anapanga kulowetsako chuma ndi imeneyo. Ndipo iwo amene anapanga kwabwino, kuyiyako chuma kwabwino, Iye anawapatsa iwo zopindula. Koma pamene munthu mmodzi anati, "Ine—ine ndinangoyisunga iyo. Ine—ine sindimafuna kuti nditengerepo mwayi uliwonse pa iyo. Ine—ine—ine ndinaiyika iyo mthumba mwanga. Kapena, ine ndinayikwirira iyo penapake." Ndiye Iye anatenga iyo imene Iye anaipereka kwa iye, ndipo anayipereka iyo kwa mmodzi amene anapeza zopindula zambiri, amene anayilowetsa iyo ku kulowetsako chuma kwabwino. Ndipo ndiyo njira ya Ambuye wathu yochitira zinthu.

33 Tsopano, koma ngati mumati muyike chuma mu chinachake chimene inu mumafuna kuti mukhale otsimikiza, inu mungapeze kampani ina yabwino, yodalirika yomwe yatsimikiziridwa kuti iyo idzalipira bwino. Tsopano, ndizo zabwino, kulowetsako chuma kokhazikika. Inu mutatha kuifufuza kampaniyo, inu

mukudziwa mbiri yake, mwayankhula ndi winawake yemwe anachitapo malonda ndi kampani iyi, ndi kumva umboni wa aliyense, "Ndi handiredi peresenti. Iwo nthawizonse amakhala olondola pa dontho ndi phindu lawo. Ndipo—ndipo ili ndi gwero lalikulu kumbuyo kwake, mwakuti kampaniyo siyingashote ndalama." Ndipo ndizo zabwino, kuyikako chuma kokhazikika. Ndipo tsopano, kudutsa mmoyo wonse, anthu akhala akuphunzitsidwa zimenezo.

34 Tsopano ife tikuyankhula usikuuno pa Lemba, la mnyamata wamng'ono wa Chihebri, yemwe anali—mtundu wolemera wa mnyamata. Iye mwinamwake anachokera ku nyumba yabwino kwenikweni, sindikukaika. Umboni wake umasonyeza kuti iye amabwera kuchokera ku—nyumba yabwino. Iye amatchedwa, mu Baibulo, "mnyamata mwini chuma." Ine ndisintha izo usikuuno, pang'ono pokha, ndikuti, "mnyamata wamalonda wolemera," chifukwa iye anali ndi bizinezi, ndipo iye anali ndi chidwi ndi—ndi bizinesi. Ndipo sindikukaikira atate ake anali mwamuna wabizinesi wochita bwino, kapena iye mwinamwake sakanakhala ndi zomwe iye anali nazo. Koma iye analeredwa kuti—kuti adzakhale mwamuna wamalonda.

35 Ndipo iye anawona chinachake mwa Mnyamata wamng'ono uyu waku Galileya, Mneneri wamng'ono uyu Dzina lake Yesu waku Nazareti. Mosakaika iye anali atamumva wansembe wake akuyankhula za Iye, ndipo mwinamwake akumutsutsa Iye. Koma pamene iye anapanga kuyang'ana kwake koyamba pa Ambuye Yesu, panali chinachake chokhudza Iye chimene chinali chosiyana ndi munthu wina aliyense.

36 Ndipo ine ndikunena izi, ngati Mkhristu, izo ndithudi sizinasinthe. Ife tiri nawo azafioloje akuluakulu mdzikoli, konsekonse mdziko, ife takhala nawo iwo kwa zaka masauzande, amene angakhoze kulozera kwa ife ka—kachikhulupiriro. Ndipo iwo amaphunzitsidwa mu tizikhulupiriro timeneto, ndi mpingo umene—umene uli mpingo wokhazikika-bwino. Koma izo apabe si yanga—ndondomeko yanga usikuuno ndikuikamba. Ine ndikukamba za Moyo Wamuyaya.

37 Ndipo mnyamata uyu, podziwa kuti iye anali membala wa mpingo, koma powona mwa Yesu chinachake chosiyana. Chotero iye anapatsidwa mwayi kuti alowetseko chuma, pamene iye anamupeza Yesu ndipo atawona zomwe Iye anali kuchita. Ndipo anali atawerenga Baibulo lake, ndipo atawona mwa Yesu kuti chinthu chimene iye anawamva aneneri ake atawerenga mu mpingo wake, ndi zimene izo zinali. Ndipo mosakaikira iye anali ataphunzira zimenezo. Ndiyeno pamene iye anaziwona mwa Yesu uyu waku Nazareti, yemwe ankaganiziridwa kuti anali pakati pa anthu, Mneneri, iye anawona chinachake mwa Munthu uyu chimene chinamuzindikiritsa Iye ndi Malemba.

38 Ndipo ine ndikuganiza, lero, izo sizinasinthe mochuluka

kwambiri. Owerenga Baibulo ndi okonda Baibulo, pamene ife tiwona kwenikweni mu luntha lathu, za chimene Yesu anali ndi chimene Iye ali, izo zimasintha kachitidwe kathu konse. Palibe wina wonga Iye, ziribe kanthu kuti ndi zabwino bwanji. Ife tinanena kuti ife tikumvetsa kuti Iye. . . Ife tikuganiza kuti Iye analibe maphunziro ochuluka, ndipo Iye ankayankhula ngati munthu wamba, ndipo ankavala ngati munthu wamba, ndi kumakhala ndi munthu wamba. Komabe panali chinachake chodziwika chokhudza Munthu uyu, ndipo icho chinakopa chidwi cha mnyamata uyu. Mochuluka, mwakuti, iye anali nacho chuma chonse cha mdziko, mwinamwake, chimene iye ankachisowa ndipo akanagwiritsa ntchito mu nthawi ya moyo wake, ndipo iye anali wokhutitsidwa bwino ndi zimenezo. Koma iye anawona kuti Munthu uyu ankayang'ana mtsogolo ndi kumawauza iwo zinthu zimene zinali nkudza, ndipo anadzizindikiritsa Yekha mu Lemba, ndipo Mulungu anadzizindikiritsa Yekha mwa Munthuyu.

39 Tsopano palibe munthu amene amakhala moyo, yemwe amakhala mmalingaliro ake abwino bwino, koma yemwe nthawizonse amadabwa komwe iye anachokerako, yemwe iye ali, ndi kumene iye akupita? Pakhala pali mabuku ambiri amene alembedwa, ambalume awukapo ndipo nkugwa. Koma pali Bukhu limodzi lokha limene lingakuuzeni inu yemwe inu muli, kumene inu mukuchokera, ndipo kumene inu mukupita, ndipo limenelo ndi Baibulo. Ndilo Bukhu lokhalo. Mwa mabuku abwino onse omwe tiri nawo, inu mukhoza kuwataya iwo, limodzi lirilonse. Ichi ndi Choonadi. Chirichonse chotsutsana ndi Ili si cholondola. "Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Anga sadzalephera konse. Mawu a munthu aliyense adzakhala bodza; a Mulungu adzakhala owona."

40 Ndipo pamene inu muwona chinachake chotsimikizika pamaso panu, ndipo Malemba analonjeza za tsiku limenelo, chimene Mesiya ameneyo anali woti adzakhale. Ndipo mnyamata uyu anaziwona zimenezo zikuzindikiritsidwa ndi Mulungu, ndiye zimenezo zinamupanga Yesu kukhala palimodzi wosiyana ndi munthu wina aliyense yemwe iye anayamba wamuwonapo. Chotero, iye anapatsidwa mwayi.

41 Pamene iye anamupeza Ambuye Yesu, ndipo mwinamwake anamuwona Iye mmisonkhano Yake ndi utumiki Wake, iye anathamangira kwa Iye ndipo anakagwa pansi pa mapazi Ake, kusonyeza kuti mawonedwe ake a mafikidwe anali olondola.

42 Ndipo iye anati, "Mphunzitsi Wabwino, ine ndingachite chiyani kuti ndikhale nawo Moyo Wamuyaya?" Tsopano ndicho chinthu chimene chikufunsidwa. Osati ndalama zake, kapena ayi, "Kodi ine ndingajowine mpingo Wanu, Bwana? Kapena kodi ine ndingakhale wa bungwe Lanu?" Koma, "Kodi ine ndichite chiyani kuti ndikhale nawo Moyo Wamuyaya?" Limenelo linali funsolo.

43 Ndipo iye anapatsidwa mwayi woti awulandire Iwo, koma iye anapanga chigamulo chopupuluma. Iye anali . . . anazikana izo. Iye sanakondweretsedwe nazo, pamene iye anadzapeza zimene zinkayenda limodzi ndi izo. Iye anazindikira, kuti polinga kuti achite izi, iye ankayenera kuti akusiye kutchuka kwake. Chifukwa, Yesu anali wosatchuka, wosakhulupiriridwa pakati pawo, ine mwanzeru ndinganene kuti, nainte peresenti pa handiredi ya anthu, kapena mwinamwake nainte-faivi pa handiredi amatero. Iye samakhulupiriridwa, ngati "munthu wa mzimu-woipa," ndipo ankatchedwa, ndi ambiri, "Belezebule," mdierekezi.

44 Ndipo, komabe, Malemba mwangwiro akumuzindikiritsa Iye. Iye anali atalozera mmbuyo kwa iwo, kuti, "Fufuzani Malemba, pakuti mwa Iwo inu mumaganiza kuti muli nawo Moyo Wamuyaya. Ndipo Iwo ndi Amene amachitira umboni za Ine, kapena kunena Yemwe Ine ndiri."

45 Mnyamata wa Chihebri uyu, pokhala kuti analeredwa mnyumba, ndipo ankadziwa kuti Baibulo linali nalo—linali litawauza iwo momveka bwino, Mipukutuyo, Mulungu, Yehova, anali atanena kuti, "Ngati angawuke mmodzi pakati panu, yemwe ali wauzimu, kapena mneneri, ine Ambuye ndidzazizindikiritsa Ndekha kwa iye mmasomphenya. Ndipo ngati chimene iye anena chifika pochitika, ndiye mudzamumvere mneneri ameneyo, pakuti Ine ndiri ndi iye. Koma ngati izo sizidzafika pochitika, ndiye musati mudzazimvere izo."

46 Ndicho chinenero chomveka. Ndiko kuganiza kwabwino. Ngati iye ananena izo, ndipo izo nkusachitika, ndiye ndi bodza; Mulungu sananene izo. Koma ngati iye anena, ndipo izo—izo nkuchitika, ndicho choonadi; ndipo palibe chinanso, choposa choonadi.

47 Chotero mnyamata uyu anali ataziwona izi mwa Ambuye Yesu, ndipo anadziwa kuti Iye amagwirizira mafungulo a Moyo Wamuyaya uwu, ndipo iye ankafuna Moyo Wamuyaya uwu, koma iye anakana mwayi woti apange kulowetsako chuma chake. Iye sanakondweretsedwe ndi kulowetsako chuma koteroko. Ngakhale . . .

48 Iye anazindikiritsidwa bwino bwino kuti Iye anali Mwana wa Mulungu. Anazindikiritsidwa mwangwiro. Namwali anali ataima, anabala Mwana. Iye anali atachita chizindikiro chirichonse chimene Mesiya ankayenera kuti adzachite.

49 Koma pofuna kuti amuvomereze Iye, iye ankayenera kuti achoke ku mwambo wake. Iye ankayenera kuti achoke kwa izo.

50 Ife tikufuna kuti tipereke izo kokha kwa . . . mnyamata wa Chiyuda uyu, koma izo ndi zoipa kwambiri kuti ife tikuyenera kuzizindikira izo, lero, mwanjira yomweyo. Ndi mtengo waukulu. Ife tikhoza kuthandizira kwa mipingo ya lero. Ndipo

nthawi zambiri, anthu amene amadzitcha okha okhulupirira, ndipo sakufuna kudzilekanitsa okha, ndi kupatuka ku zinthu za dziko lapansi, monga mnyamata wamng'ono uyu anafunsidwa kuti achite, kuti akhale ndi ndondomeko ya Moyo Wamuyaya. Komabe, zitatha, ife nafenso tikuziwona Izo zikuzindikiritsidwa bwino bwino ndi Lemba, kuti Ndondomekozo zikuperekedwabe kwa aliyense amene akufuna kuti awulandire Iwo.

51 Monga ine ndinanena, iye anawona chinachake mwa Yesu, panalibe munthu anali nacho, koma mtengo wake unali waukulu kwambiri mwakuti iye sanafune kuti alipire mtengowo.

52 Ndi chinthu chomwecho lero. Monga ine ndikukhulupirira, usikuuno, ine ndikhoza kukhala ndikuyankhula kwa zipembedzo zosiyanasiyana, Methodisti, Baptisti, Presbateria, Roma Katolika, Myuda wa Orthodox, Buddha, chirichonsecho, ndiwo anthu amalonda a m'mizinda. Koma pali, kwenikweni, pamene iwe uwona chinachake ndi maso ako omwe, chimene Malemba akuzindikiritsa kuti ndi choonadi; ife tingakhale anthu osaganiza bwino kwambiri, kuti, ngati ife tikukondweretsedwa nawo Moyo Wamuyaya, kuti tiwukane Iwo. Icho chingakhale a—chigamulo chopupuluma chonga chimene mnyamata uyu anapanga. Nthawi zambiri, ngakhale azibusa athu lero akupanga kulakwitsa kopupuluma komweko, ngakhale masikolala opukutidwa mu tizikhulupiriro, amene amadziwa izo A mpaka Z. Koma, kumbukirani, ansembe amenewo mu tsiku limenelo ankadziwa mipukutu, kuchokera ku A mpaka Z, nawonso, koma iwo analephera kuti awone chimene mnyamata uyu anawona.

53 Ndipo iye anali ndi chidwi mu—mwa Yesu kuti amupatse iye Moyo Wamuyaya. Koma pamene iye anadzapeza chimene icho chikanati chimutengere iye, ndiye iye sanali wokondweretsedwa.

54 Inu mukudziwa, Baibulo limatiuza ife, mu m'badwo uno umene ife tikukhalamo. Monga M'bale wathu Pearry wachisomo kwambiri apa wafotokoza kwa ife, kuti iye amakhulupirira kuti izo zinali mmasiku otsiriza. Ine ndithudi, ndimakhulupirira mokhazikika zimenezo ndi mtima wanga wonse. Ine ndikukhulupirira Lemba limazindikiritsa izo.

55 Ine ndimakhulupirira kuti—kuti—kuti sayansi imazindikiritsa izo. Asayansi amati, "Ndi maminiti atatu kuti ikwane pakati pa usiku." A—a . . . Madongosolo athu amene ife timawawona pa televizioni ndi—ndi pa wailesi, ndi—ndi momwe anthu athu akuchitira, ndi . . .

56 Monga ine ndinapangira ndemanga apa kapena kwinakwakenso, kuti izo zikundikumbutsa ine, za kutengeka konse kumene iwo amachita, izo zimandikumbutsa ine za mnyamata wamng'ono akudutsa pa manda usiku, akuyimba muluzu, kuyesera kudzipangitsa yekha kuganiza kuti iye sakuwopa, koma iye akutero.

57 Ndiro limene liri vuto ndi kutembenuza kwathu konse kumene ife tikuchita lero, za kutchuka kwathu konse kukuchitikaku. Ife tikuyesetsa kuwapanga anthu kumaganiza kuti ife sitikudziwa kuti ora liri pafupi, koma ife tikudziwa kuti ilo liri. Asayansi athu akudziwa zimenezo. Athu. . . A pentagon akudziwa. Tonsefe, ife tonse tikudziwa kuti pali chinachake chikukonzekera kuti chichitike. Inu, mukhoza kuzimverera izo mu mlengalenga momwe, ndipo ife tikudziwa kuti iyo yayandikira.

58 Ndipo Baibulo lathu limatiuza ife, mu Chivumbulutso mutu wa 3, kuti mpingo mu m'badwo uno udzazindikiritsidwa basi monga mnyamata wolemera uyu, wamng'ono, wa Chihebri, "olemera, sakusowa kanthu," M'badwo wa Laodikaya uno. Ngati papezeke pali atumiki pano, kapena owerenga Baibulo. Uno ndi M'badwo wa Laodikaya. Ndipo iwo unati, "Chifukwa ndine wolemera, ndikukhala ngati mfumukazi, sindisowa kanthu." Anati, "Kodi iwe sukudziwa kuti ndiwe watsoka, wosauka, wakhungu, womvetsa chisoni, wamaliseche, ndipo sukudziwa izo ayi." Chinthu chachisoni cha chobwereza Mwamalemba ichi ndi. . .

59 Ngati titamuwona mwamuna kapena munthu pa msewu, amene anali wakhungu ndi wamaliseche ndi womvetsa chisoni ndi wosauka, amenewo angakhale a—mawonekedwe oyipa. Palibe wina koma amene angathamangire kwa iwo mwamsanga momwe iwo akanathera, ndi kukati, "Mzanga, iwe uli maliseche. Iwe uyenera—iwe uyenera. . . Iwe ukuyalutsidwa. Lowa, mwamsanga, ndipo—ndipo—ndipo tabwera ndikupatse zovala zina. Ndipo ine ndikutengera iwe kwinakwake kuti ndikawone ngati ndingakhoze kukupezera dokotala, kuti iwo akakhoze kubwezeretsa kupenya kwako," kapena kuyesera kumuchitira chinachake munthuyo.

60 Bwanji ngati inu mutakumana ndi munthu woteroyo, ndipo iwo nkupotolokera kwa inu ndi kukuuzani inu kuti kazichitani zanu? Iwo sakudziwa nkomwe kuti iwo ali mu chikhalidwe chimenecho. Tsopano ngati inu muli mwanjira imeneyo, ndipo mukudziwa izo, izo sizingakhale zoipa kwambiri. Koma pamene inu muli mwanjira imeneyo, ndipo nkusadziwa izo, ndiro gawo loipalo. Iwe sungakhoze kuwauza iwo.

61 Ndipo Lemba ili liyenera kukwaniritsidwa, monga Malemba onse ayenera kukwaniritsidwa. Baibulo linanena kuti ichi chidzakhala chikhalidwe mmasiku otsiriza. Ndipo iwo amukana Yesu, ndipo Iye anali kunja kwa mpingo, akuyesetsa kuti alowe mkati. Anazikana izo, momveka basi monga Mhebri wamng'ono uyu anachitira. Ndipo uwu unali mpingo wa Amitundu, mpingo wa Mkwatibwi, woitanidwa atuluke, wotchedwa "mpingo wa Chikhristu" mmasiku otsiriza, koma iwo anakamuika Iye kunja pa chifukwa chomwecho chimene mnyamata wamalonda wa

Chihebri uyu anamukanira Iye pamenepo. Mtengowo unali waukulu kwambiri. Iwo sakanakhoza kuwulandira Iwo.

62 Baibulo linanena apa kuti iwo anali "olemera," anati iwo "anali osasowa kanthu." Mnyamata wamng'ono uyu anali wolemera, anali wosasowa kanthu. "Ndife chipembedzo chabwino chimene chiri ndi madongosolo aakulu omangidwa. Ife tiri nawo ubale. Ife tiri nazo zonse *izi, izo,* kapena *zinazo*. Ife takhalapo nato tizikhulupiriro tathu kwa mahandiredi a zaka. Ife takhala. Ife sitikusowa kalikonse. Musatiuze ife chirichonse cha Izo!"

63 Chabwino, ndiwo mkhalidwe wamwano kuposa momwe mnyamata uyu anachitira. Iye sanatenge khalidwe la mtundu umenewo. Baibulo linanena, kuti, "Yesu anayang'ana pa iye ndipo anamukonda iye."

64 Ine ndikudabwa lero, ngati pakati pa chisokonezo chathu chonse ndi chidziko chathu, ndipo komabe tikuyesetsa kugwira zodzinenera zathu za Chikhristu, ngati icho sichiri chikondi cha Mulungu chimene chikukakamiza utumiki kuti ukhale pa ntchitoyi. Ine ndikudabwa ngati icho sichiri chinthu chomwecho, monga apa ife tikumupeza Iye akugogoda pa chitseko, akuyesetsa kuti alowe mkati. Tsopano tikuzipeza zinthu izi, izo zonse kudutsa mmibadwo, izo zakhala ziri mwanjira iyi.

65 Tsopano, kuti tisunge nthawi, ndiyankhule za ndondomeko kachiwiri, ndipo basi mongogwirizira ndizifotokoze izi kwa inu.

66 Tsopano mnyamata wolemera uyu, iye sanapemphe kuti ajowine mpingo Wake. Iye—iye anali wa mpingo. Izo zinatsimikizira izo.

67 Yesu anati kwa iye, "Usunge malamulo. Iwe ukuwadziwa iwo. Usachite chigololo. Usabe. Usachite bodza, kunyengezera. Ndi—ndi kuchita, ndi—ndi kenako lemekeza abambo ako ndi amako."

68 Ndipo mnyamata wamng'ono uyu anatsimikizira kuti iye anali—mnyamata wabwino, wotukuka, osati zina zomwe ife tingatchule lero, a—a chigawenga. Iye anali mnyamata wa mtundu wabwino, analeredwa mu nyumba yabwino. Iye anati, "Mphunzitsi, ine ndachita izi kuyambira pamene ine ndinali mnyamata, moyo wanga wonse." Mwaona, izo zinasonyeza kuti makolo ake anali makolo abwino. Iye ankapita ku mpingo umene umakhulupirira mu kusunga malamulo. Komabe, mu mpingo, kusunga malamulo, sikunayankhebe zimene iye anaziwona mwa Yesu. Iye amadziwa.

69 Ndi kachikhulupiriro kathu ndi mpingo wathu, ndi kusunga malamulo, sizimatipatsabe ife Moyo Wamuyaya. Izo sizinatero nthawi imeneyo, ngakhalenso izo sizikutero lero. Pali chinachake chimene iwe uyenera kuchita.

70 Tsopano, ife tikupeza kuti sizinatero chifukwa chakuti iye sanali membala wa mpingo. Izo sizinatero chifukwa chakuti iye sanali wamakhalidwe abwino. Iye anali.

71 Koma ife tikhoza kukhala membala wa mpingo, ndipo amakhalidwe abwino, osapezabe Moyo Wamuyaya. Osati kuwadziwa Mawu; ena a iwo ndi azafioloje, ndi masikolala, ndi aphunzitsi a Sande sukulu, ofotokoza Baibulo, koma zimenezo sizitanthauza chirichonse. Satana amalidziwa Baibulo limenelo mwabwino kuposa aliyense wa ife. Baibulo linati, "Kumudziwa Iye ndi Moyo," osati kuwadziwa Mawu. "Kumudziwa Iye ndi Moyo." Satana nayenso amakhulupirira ndipo amanjenjemera. Koma ife tiyenera kukhala nacho chotichitikira cha imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro, kuchokera ku moyo wathu wakale, kupita ku Moyo watsopano umene umabwera mwa Khristu. Iwo umabwera kokha mwa Mzimu Woyera, Moyo watsopano.

72 Tsopano tiyeni tifufuze ena a anthu awa kutsika kudutsa mmibadwo, omwe anagwira ndondomeko iyi, ndikuwona ngati iyo imalipira kapena ayi. Ndiye ine ndikungofuna kukubweretserani inu, monga ine ndinakuuzani inu poyambirira, kuti inu muzifunsira kwa winawake pamene mukufuna kulowetsako chuma; mufufuze zomwe zimachitika, chiyani, kodi iyo ndi yolipira bwino. Inu muyenera kuchita zimenezo mu bizinesi yanuyo. Ine ndikufuna kuti ndiyankhule za ena omwe anakhalapo nayo ndondomeko iyi.

73 Ine ndikubweretsa ku tcheru chanu, usikuuno, mmbuyo ku Genesis, kwa mneneri dzina lake Nowa. Ngakhale iye anayesedwa mwanjira iliyonse imene iye akanathera, mwanjira iliyonse imene Satana akanakhoza kumuyesa iye, kuti amupangitse iye kuti asiye ndondomeko imeneyo; koma Nowa anagwiritsitsa lonjezo la Mulungu, ndondomeko ya Moyo, chifukwa Mulungu anamuuza iye kuti chirichonse kunja kwa chombo chimenecho chikanadzawonongeka, ndipo ngakhale izo zinkawoneka ngati zosazolowereka kwa anthu oganiza mwamakono a tsiku lake.

74 Ndicho chimene chimapangitsa Uthenga lero. Ndi kusazolowereka, chifukwa Mulungu ndi wosazolowereka. Mawu Ake amatanthauziridwa mosazolowereka kwa chimene ife nthawizina timawatanthauzira Iwo.

75 Koma, monga ine ndanena kale, Mulungu samasowa aliyense kuti atanthauzire Mawu Ake. Iye amachita kutanthauzira Kwake Kwake mwa—popangitsa kuchitika zinthu zimene Iye anati Iye akanadzachita. Iye amatanthauzira Mawu Ake Omwe. Iye samasowa kutanthauzira kwathu. Ndi, kutanthauzira kwathu ndi maganizo athu opangidwa ndi anthu omwe ife timakhala nawo Iwo.

76 Pamene Mulungu anati, "Pakhale kuwala," ndipo apo panali kuwala. Zimenezo sizimasowa kutanthauzira ayi.

77 Mulungu anati, "Namwali adzaima," ndipo iye anatero. Zimenezo sizisowa kutanthauzira kulikonse.

78 Yesu anati, "Mwana wa munthu akupita ku Yerusalemu ndipo akukaperekedwa mmanja a munthu wochimwa. Iwo adzamupachika Iye, ndipo pa lachitatu Iye adzawukanso kachiwiri." Zimenezo sizikusowa kutanthauzira ayi.

79 Iye anati, "Kanthawi pang'ono ndipo dziko silindiwonanso Ine; komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumalekezero a m'badwo, mpaka ku chimaliziro." Iye ali pano. Izo sizikusowa kutanthauzira kulikonse. Ilo ndi lonjezo Lake.

80 "Ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita. Iye amene akhulupirira mwa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita." Zimenezo zikupezeka mu Yohane Woyera 14:12. Ndipo ife tikudziwa kuti izo nzoona, kotero izo sizikusowa kutanthauzira kulikonse.

81 Nowa, ali ndi Mawu a Mulungu, anagwiritsitsa kwa Iwo, chifukwa iye amagwirizira ndondomeko ya inshuranse ya Moyo, chitsimikizo cha Moyo. Iye anagwiritsitsa ndondomekoyo. Ndipo iye anali nthumwi ya ndondomekoyo, ndipo iye amapita kulikonseko. Koma chifukwa izo zinali zosatchuka, iye samakhoza kumupeza aliyense kuti atenge izo, basi banja lake lomwe. Iye anali . . . Yake—ndondomeko yake inkawoneka kuti inali yakutha, kwa anthuwo. Izo zinkawoneka kuti zimatsutsana ndi kulingalira kwa sayansi kwa tsikulo. "Mvula kutsika kuchokera kumwamba."

82 Iyo inali isanavumbe pa dziko lapansi, inu mukukumbukira. Dziko linkaima molunjika. Ife tikhoza kutsimikizira zimenezo lero, kuti ilo nthawiyina linkaima mwanjira imeneyo. Ndipo Mulungu ankathirira zomera kudzera mu mthirira, kuchokera mu akasupe wa m'nthaka.

83 Tsopano sayansi, mu tsiku limenelo, mwinamwake anali anzeru kwambiri kuposa momwe iwo aliri tsopano, chifukwa iwo ankamanga zoimikidwa ndi mapiramidi, ndi—ndi zina zotero, zinthu zimene ife sitingakhoze kuyesera kuti tizichite lero. Ife tiribe mphamvu zimene zingakhoze—zingakhoze kuchita zimenezo, koma iwo ankamanga zimenezo. Ndipo ine ndikuganiza mwinamwake iwo ankapita ku mwezi ndi makwerero kapena chirichonse chimene iwo anali nacho mu tsiku limenelo.

84 Yesu anati, "Monga izo zinali mmasiku a Nowa," chitukuko china chofanizidwa ndi chimenecho, "chomwechonso izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu."

85 Ife tinawona kuno posachedwapa kumene iwo anakumba zomangidwa zamakono kuno mu Mexico wakale, alibe mbiriyakale ya izo, nkomwe. Mwaona, izo zikhoza kukhala zochokera ku m'badwo wina umene unadutsapo.

86 Yesu anati, "Monga izo zinali mu tsiku limenelo," munthu wanzeru, waluntha. Koma ngati izo zinalipo, ndiye padzakhala ndondomeko ya Moyo idzaperekedwe kwa anthu. Iye ananena chomwecho.

87 Ndipo, Nowa, iye mwina sangakhoze kufotokoza. Monga sayansi inanena, "Ife tikhoza kutenga zida ndi kutsimikizira kuti kulibeko mvula kumwamba uko. Bwana, inu mwasokonezeka mmalingaliro anu." Komabe iye anadziwa kuti Liwu limene linkayankhula ndi iye anali Mulungu.

88 Chotero ngati Mulungu anati, "Panali madzi amene amabwera kuchokera mmwamba," ngakhale kunalibeko madzi, Mulungu ndi Elohim, Mmodzi wokhalapo-Yekha. Iye ndi Mmodzi Wokwanira mu Zonseyo. Ngati Iye anati, "Kukhoza kukhala madzi kumwamba uko," Iye ndi wokhoza kuwaika madzi kumwamba uko, kuti asunge Mawu Ake.

89 Atate athu Abrahamu, amene ali atate wa mafuko ambiri, ngati patapezeka kuti pali anthu Achiyuda akhala pafupi, akudabwa momwe Amitundu anabweretsedweramo, Abrahamu anali atate wa mafuko ambiri, "Ndipo iye sanadzandime pa lonjezo la Mulungu kupyolera mu kusakhulupirira," iye anagwiritsitsa ku ndondomekoyo. Mulungu anali atamupangira iye lonjezo, kuti akhale atate wa mafuko ambiri, osati mafuko Achihebri okha, koma mafuko ena, kuti iye akanadzakhala atate ake.

90 Zindikirani, monga iye anachitira, lonjezo limene Mulungu anamupatsa iye linali lopupuluma, mowonjeza. Iye anali usinkhu wa zaka sevente-faivi zakubadwa, ndipo Sarah anali sikisite-faivi, iye asanalandire lonjezolo. Koma iye anadzilekanitsa yekha kwa osakhulupirira, chifukwa iye ankadziwa kuti iye anali wolandira wa chirungamo mwa chifuniro cha Mulungu, ndipo ziribe kanthu kuti zatenga motalika chotani!

91 Mwinamwake mwezi woyamba unadutsa ndipo iye anati kwa Sarah, "Kodi iwe ukumverera bwanji?"

"Palibe kusintha."

92 Anati "Ife tidzakhala naye mwanayo, mulimonse. Mulungu wanena chomwecho. Kazipitirira kupanga tinsapato. Ukonzekeretse chirichonse. Mulungu anati ife tikhala naye iye. Izo zikukhazikitsa izo."

Chaka choyamba chinadutsa. "Wokondedwa, kodi iwe ukumverera bwanji?"

"Palibe kusintha."

93 "Chabwino, icho chidzakhala chozizwitsa chachikulu kuposa momwe zikanakhalira ngati izo zikanachitika mwezi woyamba."

94 Mwaona, iye anali pafupifupi zaka teni atadutsa kusintha kwa thupi pamene lonjezolo linaperekedwa. Iwo analibe ana. Iye anali wosabereka, ndipo iye anali chumba. Chotero iwo . . . Koma iye anagwiritsitsabe ndondomeko imeneyo, chifukwa iyo inali Mawu a Mulungu, lonjezo. Iye sanali woti alekana nayo iyo. Ndipo Baibulo linanena, kuti, "Abrahamu sanadzandime pa lonjezo la Mulungu kudzera mu kusakhulupirira; koma anali wamphamvu, akupereka matamando kwa Mulungu; akudziwa ichi, kuti, Iye ndi wokhoza kuchita icho chimene Iye analonjeza kuti adzachichita." Chotero mwanayo anabadwa, chifukwa chakuti iye anagwirizitsitsa—ndondomekoyo.

95 Nowa anagwiritsitsa ndondomeko yake, ndipo iyo inapulumutsa moyo wake. Kumeneko kunali kulipirako. Osati moyo wake wokha, koma moyo wa banja lake; unalipiridwa, powapulumutsa iwo.

96 Tiyeni tiyankhule kwa wolowetsa chuma wina mu inshuranse ya Moyo Wamuyaya iyi. Daniele mneneri, pamene monga ife tingazitchulire izo . . . Ngati inu mungakhulukukire izo, monga kafotokozedwe ka chidziko; ine ndisanene izo, ine ndikuganiza, pano pa guwa. Ndiyo njira yokhayo yomwe ine ndimaidziwa kuti izo zindiyendere, "pamene zinthu zandivuta." Mfumu Nebukadinezara anali atabwera umo ndipo anawatenga ana a Israeli chifukwa iwo anali atachoka kwa Mulungu. Iwo anali; akuchitabe nsembe zawo zonse.

97 Pamene Mulungu anawafunsa iwo kuti apereke anaankhosa ndi ng'ombe, ndi zina zotero, munthu, Myuda wabwino, anayenda chotsika msewu, ali ndi ng'ombe yonenepa kapena—kapena—kapena mwanawankhosa wamng'ono mkhwapa mwa nkono wake, pa tsiku la chitetezero, amapita uko kuti akapereke izo kwa tchimo lake, iye amakhala wodzipereka pamene iye akumupha mwanawankhosa ameneyo, ndipo wansembe ankamubaya iye, ndipo iye ankakwezera manja ake pa iye, akudziwa kuti moyo wachotsedwamo kuti apulumutse moyo wake, iye amakhala wodzipereka pochita zimenezo. Ndipo bola ngati iye anali woonamtima, izo zimakhala zabwino, koma nthawi inafika pamene icho chinadzakhala mwambo wa pa banja, ndiye Mulungu anati, Iye anatumiza mneneri powonekera, dzina lake Yesaya, Iye anati, "Nsembe zanu, maphwando aulemu, zikununkha m'mphuno Zanga."

98 Ndi pamene ife anthu tafikapo. Ife tajowina mpingo. Chimene, chiri chabwino, ife timachita zinthu zimenezo. Koma, inu mukuti, kodi ndinu Mkhristu? "Ndine wa Methodisti. Ndine wa Baptisti. Ndine wa Presbateria, Pentekoste, kapena chinachakenso." Ndi mwambo. Palibe kulowamo,

moonamtima, panonso. Iwo sangasunthire mmwamba, kuyenda nawo Malemba ndi zinthu. Iwo amangokhala moyo uliwonse umene iwo akufuna. Ngati iwo ali ndi m'busa akuyesera kuti awakonze iwo, iwo amamuchotsapo iye. Iwo alibe chochita naye iye ngati iye sangakhoze kubweretsa Hollywood mu mpingo; maphwando, maphwando a bunco, maphwando a msuzi, ndi china chirichonse; kuwalola akazi azichita mulimonse momwe iwo akufunira, ndi kumavala mulimonse momwe iwo akufunira, mopanda makhalidwe, chirichonse. Kukopa kofuna kugonana kwakhala a—kachitidwe kamakono. Ndi chamanyazi.

99 Yesu ananena, kwa mkazi uja. Inu mukhoza kukhala wangwiro monga inu mungakhoze kukhalira, koma inu mudzakayankha chifukwa cha chigololo pa tsiku la chiweruzo, inu mukumavala zovala zimenezo. Yesu anati, "Aliyense amene ayang'ana pa mkazi, namukhumbira iye, wachita naye kale chigololo iye mu mtima mwake." Ndipo ziribe kanthu kuti ndinu wosalakwa bwanji, wochimwa ameneyo adzakayankha za chigololo, ndipo ndinu yemwe munapereka izo. Inu Akhristu, kodi inu simukuchita manyazi? Inu muyenera muzichita ngati ana aakazi a Mulungu.

100 Ndipo inu amuna, mamembala a mpingo, madikoni, ngakhale mpaka azitumiki, amene mumaloleza akazi anu kuti azichita zimenezo, inu muyenera kukhala ana aamuna a Mulungu. Zimenezo sizikumveka ngati khalidwe la mwana wa Mulungu wokhala ndi chikhalidwe cha Atate ake mwa iye. Kuwopa kuti munene chinachake chifukwa bungwe lingakutulutseni inu panja. Uko nkulondola.

101 Daniele analinga mu mtima mwake kuti iye sanali woti ayipitse chuma chimene analowetsamo. Iye analinga, "Zinalibe kanthu zomwe dziko, momwe mfumu inali yolemera, ndi kuchuluka kwa momwe angayesere kundijejemetsa ine ndi zinthu za mdziko, ine sindichita zimenezo. Ine sindidzaipitsa chuma changa chimene ndalowetsamo."

102 O dziko la Chikhristu, musayipitse kuika chuma kumene inu mwapanga mu Moyo Wamuyaya. Inu mudzawononga izo.

103 Daniele analinga kuti iye sakanati achite zimenezo. Izo zinamulipira, populumutsa moyo wake pamene iye anaponyedwa mdzenje la mikango. Kuyikamo chuma kwake ndithudi kunapindula.

104 Ana Achihebri anali wotsimikiza kuti iwo sakanakhoza kupembedza fano. Ndipo izo zinalipira, populumutsa moyo wawo mu ng'anjo ya moto.

105 Kenako panadzabwera Simoni Petro, Mfarisi wabwino amene anaphunzitsidwa ndi abambo ake, kuti tsiku likanadzabwera kuti—kuti kudzabwera Mesiya. Monse kudutsa mibadwo, anthu Achiyuda anali akuyembekezera zimenezo. Ndipo sindikukaikira kuti abambo ake anali atamuuza iye,

"Mwana . . ." Ine—ine ndinawerenga nkhani yaing'ono nthawi ina, ya iyo, mwina inali yopeka. Ine sindikunena kuti izo zinali zovomerezeka.

106 Koma iye anati, "Ine ndayembekezera nthawi ya kudza kwa Mesiya." Ndipo anati, "Ine—ine—ine ndikudziwa kuti nthawi imeneyo isanafike, padzakhala mitundu yonse ya timalingaliro, tinthu tabodza tizidzachitika. Koma, mwana, monga wa Chihebri, ife timaphunzitsidwa, monga Ahebri, kuti tiziwakhulupirira aneneri athu, pakuti Mawu a Ambuye amadza kwa aneneri, ndipo iye yekha. Ambuye anati, 'Ine sindichita kanthu kupatula Ine nditaululira izo kwa aneneri Anga poyamba.' Ndipo Mesiya uyu, molingana ndi Mose, 'Ambuye Mulungu wanu adzautsa mneneri pakati panu, wa abale anu, wonga ine.' Ndipo Mesiya sadzakhala wophunzira. Iye sadzakhala chipembedzo. Iye adzakhala mneneri, ndipo Mawu a Ambuye adzakhala ndi Iye."

Andreya anali atamva Yohane akuyankhula za mmodzi woteroyo akubwera, "M'batizi."

107 Komano, tsiku lina, Simoni mwiniwake anayenda kupita mu Kukhalapo kwa Yesu uyu waku Nazareti. Ndipo mwamsanga pamene Iye anayang'ana pa iye, Iye anati, "Dzina lako ndiwe Simoni, ndipo ndiwe mwana wa Yonasi." Iye anatulutsa ndondomeko mwamsanga ndithu. Iye anadziwa kuti ameneyo anali Mesiya. Limenelo linali Lemba lotsimikiziridwa la tsiku lake, Mesiya. Kodi enawo analephera bwanji kuti aziwone izo?

108 Panali mmodzi atayima, dzina lake Filipo, amene anapita pafupifupi mamailosi fifitini kuzungulira phirilo, kwa munthu wotchedwa Nataniele. Iwo ankachita zophunzira Baibulo pamodzi. Mwinamwake zokambirana zawo zinali chinachake monga chonchi, pamene iye anamupeza iye pansi pa mtengo, akupemphera. Iye anati, "Nataniele." Ndithudi, pokhala njonda imene inkamutsatira Yesu; munthu aliyense wotsatira Yesu amakhala njonda. Chotero iye anamupeza iye akupemphera; iye—iye anayembekezera kanthawi. Koma inu mukuzindikira, iye sanalankhule naye konse iye za munda wake wa azitona kapena zina zotero. Iye anapita molunjika ku chandamale, "Bwera, udzawone Yemwe ife tamupeza: Yesu waku Nazareti, mwana wa Yosefe."

Anati, "Tsopano, kodi pangakhale chirichonse chabwino chochokera ku Nazareti?"

Iye anati, "Bwera, udzawone."

109 Ndiro yankho labwino kwambiri limene munthu aliyense angakhoze kupereka kwa mzake. "Bwera, udzadzipezere wekha. Osangokhala pakhomo ndi kumatsutsa. Bwera, udzafufuze izo wekha."

110 Pa msewu akuzungulira, zokambirana zawo mwinamwake zinali chonchi. Mwinamwake Nataniele anati, "Iwe ukudziwa,

ife takhala tikumuyembekezera Mesiya, kwa zaka. Inu mukudziwa, Filipo, momwe ife taphunzirira izi. Bwanji, ine ndikukhulupirira ngati Mesiya akubwera, Mulungu adzakokera makonde a Kumwamba ndi kulola makonde aakulu adzatsikire pansi, makwerero pomwepo pa (athu) bwalo lalikulu la kachisi kumene Kayafa wansembe wathu wamkulu ali, ndipo Iye adzati, 'Ine ndiri pano."' Mukuona? Koma umo si momwe Lemba linanenera kuti Iye akanadzabwerera.

111 Iye adzabwera kokha momwe Lemba linanenera. Iye anabwera mwa mneneri chimodzimodzi monga Mose anachitira, munthu wamba, woweta nkhosa.

112 Zindikirani, ndipo pamene iye anadzabwera mu Kukhalapo kwa Mesiya, ndipo Iye anali mu mzere kapena kupempherera wodwala, kapena chirichonse chimene Iye anali kuchita. Ife tikupeza kuti Mesiya akuyang'ana pa iye, ndipo anati, "Taonani M'israeli mwa yemwe mulibe chinyengo."

113 Tsopano inu mukhoza kuganiza kuti zinali chifukwa iye anali atavala mwanjira imeneyo. Koma, kumbukirani, anthu onse Akummawa ankavala mofanana, mpango ndi ndevu, zina zotero. Inu mukukumbukira, Yesu anayenda nawo iwo, aponso, pa msewu waku Emmau, utali wa tsiku lonse, chitachitika chiukitsiro Chake, ndipo iwo sanamudziwe nkomwe Iye. Iye anali atavala mwanjira yomweyo.

114 Chotero ife tikupeza kuti mu Kukhalapo kwakukulu uku kwa Iye, iye anati, "Rabbi." Mhebri wabwino wamng'ono uyu anati, "Rabbi, ndi liti pamene Inu munandidziwa ine? Ndi liti pamene Inu munayamba mwandidziwa ine, kundidziwa ine kuti ndine—wachi Israeli, ndi woona mtima, mbiri imene ine ndiri nayo? Inu simunayambe mwandiwonapo ine kale. Zinakhala bwanji kuti Inu mundidziwe ine?"

115 Ndipo Iye anati, "Filipo asanakuitane iwe, pamene iwe unali pansi pa mtengo, Ine ndinakuwona iwe."

116 Iye anatulutsa ndondomekoyo. Anagwa pa mapazi Ake monga mnyamata wina uyu anachitira, anati, "Rabbi, ndinu Mwana wa Mulungu. Ndinu Mfumu ya Israeli." Dzina Lake ndi lachisavundi lero.

117 Pali mkazi wamng'ono, ine ndikhoza kuyankhula za iye chifukwa cha madona aima pafupiwa. Dona wamng'ono uyu sanali monga inu. Iye anali ndi chomutsutsa iye—za khalidwe lake, mpingo umatero. Mwinamwake mwana wina wamng'ono anakanidwa pa msewu, wolakwa. Mwinamwake makolo ake sanamusamalire iye. Iye anali theka Myuda ndi Wamitundu; iye anali Msamaria.

118 Kumbukirani, pali mitundu itatu yokha ya anthu, ngati Lemba lathu likulondola.

119 Ndipo Mulungu andikhulululukire ine pongonena kuti "ngati" Ilo likulondola. Ilo likulondola. Ndi Mulungu Mwiniwake. "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati." "Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse."

Chotero dona wamng'ono uyu akukanidwa.

120 Choyamba, ine ndikhoza kufotokoza anthu a Hamu, Shemu ndi Yafeti. Tsopano ife, Amitundu, ife tinali achikunja mmasiku amenewo, ife tinali kupembedza mafano, koma Myuda ndi Wamitundu anali kuyembekezera Mesiya. Ndipo Iye amangobwera kwa iwo amene akumuyembekezera Iye.

121 Nthawizina lero, ife timati tikumuyembekezera Iye, ndipo timayikamo mamillioni ndi mabillioni a madola mu zinthu, ndi kumanga malo ndi zinthu. Ine ndikudabwa. Ndipo amishonare akufa ndi njala pa kuminda, ine ndikuwadziwa iwo, kunja uko usikuuno akulalikira, opanda nsapato. Ife timaika mamillioni ndi mamillioni a madola ku zamkhutu, ndiyeno, bwanji, machitidwe athu omwe amatsutsa umboni wathu.

122 Koma apa mkazi wamng'ono uyu, monga ife tikumudziwira iye, iye anali Msamariya. Yesu anali pa ulendo Wake waku Yeriko, kumene kuli kumusi kwa Yerusalemu. Koma Iye anapita mozungulira ku Samaria ndipo anabwera ku mzinda wotchedwa Sukari, ndipo anawatumiza ophunzira kuti akagule zitumbuwa, chakudya. Ndipo pamene iwo anali atapita, mkazi wamng'ono uyu anabwera kuti adzatunge madzi, ndipo Iye—Iye anati kwa iye, "Ndibweretsere ine akumwa."

123 Ndipo iye anayang'ana pozungulira, kumuwona Iye pokhala Myuda, iye anati, "Si mwambo wake kuti Inu mundifunse ine zimenezo." Anati, "Ndinu Myuda."

124 Iye anati, "Koma ngati iwe ukanadziwa Yemwe iwe ukuyankhula naye, iwe ukanandipempha Ine akumwa. Ine ndikupatsa iwe madzi amene iwe sumabwera kuno kudzatunga."

125 Chotero kukambiranako kunapitirira, za chipembedzo, potsiriza Iye anakhudza moyo wake. Iye anati, "Pita ukamutenge mwamuna wako ndipo mubwere kuno."

Iye anati, "Ine ndiribe mwamuna."

126 Anati, "Iwe wanena zoona. Iwe wakhala nawo faivi, ndipo amene iwe ukukhala naye tsopano si mwamuna wako."

127 Tsopano masiku pang'ono zisanachitike zimenezo, aphunzitsi ndi a rabbi a tsiku limenelo, amuna amene ankayenera kudziwa bwinoko, anati, "Iye ndi Belezebule. Iye amachita zimenezo ndi mzimu woipa." Iwo ankayenera kuti akawayankhe osonkhana awo. Chotero iwo anapangana, anati, "Iwo ndi mzimu woipa."

128 Ndipo Yesu anati, “Ine ndikukhulukirani inu chifukwa cha zimenezo,” chitetezero chinali chisanapangidwe. “Koma pamene Mzimu Woyera udzabwera kudzachita chinthu chomwecho, kudzayankhula motsutsa Iwo sizidzakhululukidwa konse,” ndipo ife tikudziwa izo zinachitika pamene Tito, iwo atatha kuwukana Mzimu Woyera, Tito anatentha kachisi ndipo anawabalalitsa Ayuda kupita ku dziko lonse lapansi. Ndipo iwo tsopano akungosonkhana kachiwiri, akukwaniritsa Lemba.

Tsopano, zindikirani, tsopano mkazi wamng’ono uyu.

129 Pamene, Ayuda awo anawona izo zikuchitidwa, ndipo anazitcha Izo, “mzimu woipa, mzimu wosayera,” Baibulo linati, “kuwutcha Mzimu wa Mulungu, kumachita ntchito, Mzimu wosayera, mdierekezi,” monga wam’bwebwe kapena munthu wina woipa.

130 Ndiyeno, mwamsanga, mkazi uyu anadziwa mosiyana. Pamene Iye anati, “Pita ukamutenge mwamuna wako.”

Iye anati, “Ine ndiribe aliyense.”

131 Iye anati, “Iwe wanena zoona, chifukwa iwe uli nawo faivi, ndipo amene iwe ukukhala naye, si mwamuna wako.”

132 Tayang’anani pa izi. Mwamsanga iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri.” Kumbukirani, iwo anali asanakhale nawo aneneri kwa pafupifupi zaka faivi handiredi. Malaki anali mneneri wotsiriza wa Chihebri. “Ife, ife tikudziwa kuti Mesiya akubwera, ndipo ichi chidzakhala chizindikiritso cha Mesiya. Ife tikudziwa, pamene Iye adzabwera, ichi ndi chimene Iye ati adzachite.”

Yesu anati, “Ine ndine Iye amene akuyankhula ndi iwe.”

133 Ndipo iye anatenga ndondomeko. Uh-huh. Ndipo mu mzinda iye anapita, kuti akafalitse Uthenga wabwino, kuti iye anali atamupeza Mesiya. Iye anali nawo Moyo Wamuyaya chifukwa iye anali atakhulupirira pa Iye. Iye anadziwa bwanji? Iye anawona kuzindikiritsidwa kwa Lemba kkuwonetseredwa ndi Iye.

134 “Ife tikudziwa kuti, pamene Mesiya adzabwera. Zaka foro handiredi ife sitinakhale naye mneneri, ndipo, pamene Iye adzabwera, ameneyo adzakhala munthu wotsatira powonekera. Tsopano pamene Iye adzabwera, ife tidzamudziwa Iye, ndipo Iye ali woti adzachite chinthu chomwecho.”

135 Anati, “Ine ndine Iye.” Iye anatenga ndondomeko. Iye anali ndi chidwi ndi zimenezo.

136 Nikodemo. Mphindi pang’ono, potseka tsopano. Nikodemo, rabbi, bambo wa pafupifupi usinkhu wa zaka eyite. Iye anali atakhutitsidwa kuti panali chinachake chokhudza Yesu chimene chinali chosiyana ndi munthu wina, chotero iye ankafuna ndondomeko. Kotero iye anabwera usiku, kudzatenga

ndondomeko, ndipo iye anapeza bankiyo ili yotsegula kuti achite malonda. Uh-huh.

137 Iyo nthawizonse imakhala yotsegula. Iyo imakhala yotsegula ku phwando. Iyo imakhala yotsegula pa msewu. Iyo imakhala yotsegula paliponse pomwe pali aliyense wokonzeka kuchita malonda, ndondomeko iyi ndi amene waitenga iyo.

Iye anapeza kuti banki ndi yotsegula. Iye anatenga ndondomeko.

138 Tsopano ife tikudziwa, mu Luka 24:49, Yesu atatha kuwasankha ophunzira Ake, iwo anali atagwirizira ndondomeko ya Moyo Wamuyaya. Chotero tsopano, inu mukudziwa, mu ndondomeko ya inshuranse yachizolowezi, iwo nthawizonse amalipira zopindula. Chotero iwo anali atavomerezedwa kale ndi kusankhidwa ndi Yesu, kotero iwo anapita mpaka ku Yerusalemu, akuyembekezera mpaka Tsiku la Pentekoste, kuti akapeze zopindula zawo. Ndipo zinapindula, ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi mphamvu kuti akamuwonetsere Yesu Khristu.

139 Methodisti, Baptisti, Presbateria, Orthodox, aliyense yemwe inu muli, amene mumadzinenera kuti ndinu Akhristu, bwanji inu simukuchita chimodzimodzi? Inu mukukhulupirira pa Yesu Khristu ndipo mwakhala chiwalo cha mpingo, bwanji inu simukupita mpaka ku Pentekoste, kukatenga zopindula zanu, mphamvu ya Mzimu Woyera! Amene anali ndi ndondomeko awo anakatengako izo. Inu mukhoza, inunso, ngati inu mukukhulupirira izo ndi kukhulupirira izo kwenikweni.

140 Petro akuyankhula kwa iwo, anati, "Lonjezo liri kwa inu ndi ana anu, kwa iwo amene ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana." Iwo ankafuna kuti adziwe choti achite. Iye anati, "Lapani, mmodzi aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera." Ilo linali lonjezolo.

141 Kotero ngati inu mwangokhala wovomereza, usikuuno, ndipo inu simunatengepo zopindula zanu, bwanji inu osabweretsa ndondomeko yanuyo, usikuuno, ndiloleni ine ndiyankhule ndi inu kanthawi pang'ono. Gwadani ndi ine kwa maminiti pang'ono ndipo mupeze ngati izo siziri chomwecho. Mukhale odzipereka pa izo. Izo zidzalipira pakali pano, ngati mukugwiritsitsa kwenikweni ndondomekoyo. Iye adzaizindikira ndondomekoyo, chikhulupiriro chanu, ngati mukunena kuti chiri mwa Mulungu. Ngati icho chiri mwa Mulungu ndi mu Mawu Ake, ndipo osati mu mpingo wina kapena kachikhulupiriro ka chipembedzo, koma kungokhulupirira mwa Yesu Khristu, izo zidzalipira. Iye amadziwa ndondomeko Yake Yomwe.

142 Kubweretsa wochita wina, kwa mphindi pang'ono chabe. Panali Mhebri wina wolemera amene anakumana ndi Yesu tsiku lina itachitika imfa Yake, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro.

143 Ngati pangakhale Mhebri pano, usikuuno, kapena aliyense yemwe inu muli, Iye kupachikidwa si chowiringula chirichonse chifukwa inu mukhoza kukumanabe naye Iye pomwe pano, chimodzimodzi basi monga—monga mnyamata mwini chuma anakumana naye Iye. Ngati inu mukufuna ndondomeko, Iye ali pano kuti achite malonda.

144 Panali munthu dzina lake Saulo, ndipo iye anaphunzitsidwa mu zophunzitsa zazikulu zonse ndi miyambo ya anthu ake. Gamalieli anali mphunzitsi wake, mmodzi wa aphunzitsi Achihebri abwino kwambiri a nthawiyo. Ndipo Sauli anali wodzipereka kwambiri wa zimenezi, mpaka iye anamugenda Stefano, kapena kumuchitira umboni Stefano, kapena anavomereza izo. Anagwirizira zikhotho za iwo, pamene iye ankavomereza, pakuti anali nawo ulamuliro kuchokera kwa wansembe wamkulu kuti awaponyere anthu onsewo, a ndondomeko imeneyo, mu ndende, chifukwa iye anali atawuzidwa ndi akulu ake, kuti, "Munthu uyu sanali mneneri. Panalibe kanthu kwa Munthu uyu koma wosalongosoka." Ndipo iye anali ndi makalata mmatumba mwake, akupita uko, chifukwa iye anamva kuti kunali ena kumusi ku Damasiko, anali ndi ndondomeko imeneyo. Ndipo iwo anali ndi chidwi pa izo, ndipo iwo anali akuchita kwenikweni zinthuzo.

145 Ndipo wansembe wamkulu anamuuza iye, "Saulo, ndiwe munthu wodzipereka. Tenga ulamuliro uwu, kuchokera kwa ine, upite kumusi uko ndipo ukamange mmodzi aliyense wa iwo, chifukwa iwo si kanthu koma wosalongosoka, palibepo kanthu kwa iwo. Upite kumusiko ndipo ukawamange iwo, ndipo ukawaponyere iwo mu ndende. Iwe uyenera kuti ukawaphe iwo, ukawaphe iwo, izo ziri bwino. Upite ukawatenge iwo!"

146 Saulo anati, "Ulemu wanu, bwana, abambo oyera, ine ndipitako." Kumusi iye anapita.

147 Ali panjira yake wa kumeneko, iye anali akuyenda cha m'ma leveni koloko masana, akuyandikira mzindawo. Zonse mwadzidzidzi, kuchokera mmiyamba munabwera Lawi la Moto, linamukanthira iye pansi. Ndipo iye anadzuka kuti ayang'ane, ndipo apo panali Lawi la Moto lija patsogolo pake.

148 Tsopano kuti nditsimikizire izo kwa inu. Iye anali Mhebri, ndipo iye sakanati apembedze chirichonse kapena kuchitchula chirichonse Ambuye, kupatula ngati iye atadziwa kuti icho chinali Ambuye. Ndipo iye anadziwa, monga mphunzitsi pansi pa Gamalieli, kuti Mngelo wa Ambuye, yemwe anali Logos yomwe inatuluka kuchokera kwa Mulungu, amene anali Khristu amene anawatsogolera iwo kudutsa mchipululu, anali mmawonekedwe a Kuwala, Lawi la Moto. Ndipo pamene Iko

kunamukanthira iye pansi, ndipo iye anayang'ana mmwamba ndipo anakuwona Iko pamenepo, iye anati, "Ambuye." Tsopano, iye sibwenzi atatchula chirichonse koma Chimenecho, Ambuye. Koma, pokhala wa Chihebri, iye anadziwa kuti Ameneyo anali Yehova. Ndi chifukwa chake iye anali nalo vumbulutso, amakhoza kunena kuti Yesu wa Chipangano Chatsopano anali Yehova wa Chakale. Limenelo linali vumbulutso lake, chifukwa iye anali atamuwona Yehova. Ndipo iye anati, "Ambuye, Ndinu Yani?"

149 Iye anati, "Ine ndine Yesu, ndipo ndi kovuta kuti iwe uzimenyana ndi zisonga." Ndipo iye anatulutsa ndondomeko.

150 Mufanizitse amuna awiriwo pamodzi. M'modzi wolemera Mhebri wamng'ono amene ankafuna kuti agwiritsitse ku miyambo yawo; mmodzi wina amene anakhutitsidwa. Mmodzi wa iwo anamuwona Iye ngati munthu, kuti Mulungu anapangidwa thupi polinga kuti adzafe ndi kudzachotsa tchimo.

151 Magazi a anaankhosa ndi zinthu, moyo unali mmenemo, sukanakhoza kubwera pa wokhulupirira, chifukwa iwo ndi moyo wa mwanawankhosa, iwo ulibe solo mwa iwo, moyo wa chinyama. Koma uyu anali Mulungu Mwiniwake, ndipo, ndiye ife timadzabadwa mwa Mzimu umenewo, ndife ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, Moyo umene unali pa Nsembe yathu.

Muwafanizitse amuna awiriwo pamodzi.

152 Analiwona Ilo likutsimikiziridwa, kuti Mulungu anali mwa Khristu. Lawi la Moto lomwelo limene linawabweretsa anthu Ake kudutsa mchipululu, ndi kuwabweretsa iwo kumeneko, kuwadyetsa iwo tsiku lonse. Kumbukirani, pamene Yesu anali pa dziko lapansi, Iye anati, "Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu, ndipo ine ndikupita kwa Mulungu." Iye anali Lawi la Moto limene linkawatenga ana kudutsa mchipululu.

153 Baibulo linanena, kuti, "Mose anachiyesa chuma cha Khristu chuma chachikulu kuposa icho cha Igupto." Iye anasiya Igupto, kuti akamutsatire Khristu.

154 Pamene Iye anali kuno, Lawi la Moto lija linaimiridwa mwa Iye, Mulungu. Iye anati, "Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine. Ntchito zikukuuzani inu zomwe Ine ndikuyenera kuti ndizichita. Ngati Ine sindikuchita zimenezo, ndiye musakhulupirire izo. Koma ngati inu simungandikhulupirire Ine. . . "

Iwo anati, "Ndiwe—Ndiwe munthu ukudzipanga Wekha kukhala Mulungu."

155 Anati, "Ngati inu simungandikhulupirire Ine, ngati Munthu, mukhulupirire ntchitozo. Izo zikuchitira umboni za Ine." Mukuona?

156 Tsopano, pamene Iye anafa, anaikidwa mmanda, anauka, anakwera, apa ife tikumupeza Iye kachiwiri mu Lawi la Moto

limenelo. Iye anali atabwera kuchokera kwa Mulungu, ndipo anapita kwa Mulungu.

157 Iye akadali Mmodzi yemweyo, Mmodzi yemweyo tsopano. Zindikirani, zedi, Mmodzi yemweyo amene Iye anali.

158 Ndipo pamene Paulo, kapena Sauli pamenepo, anazindikira kuti Mulungu Yehova, Lawi la Moto la Chipangano Chakale, anali atadzitchula Yekha Yesu, iye anatenga ndondomeko yake. Iye anali atakonzekera izo pamenepo.

159 Chigamulo chopupuluma bwanji cha mnyamata wolamulira uja! Chiyani...Momwe iye ankayenera kuti...Chiyani, iye anachita bwanji zimenezo? [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi].

160 Kodi inu mungapereke chiyani posinthanitsa ndi solo yanu? Mutakhala ndi nyumba zanu zonse, ndipo inu—inu nkuzisiya izo kuti azibale anu azimenyenirana, ndi chirichonse, nanga bwanji solo imeneyo ndi kumene inu muti mudzakakhaleko? Kumbukirani, inu mudzakakhala kwinakwake, zaka masauzande kuchokera usikuuno. Iyi ikhoza kukhala nthawi yoti inu mupange chisankho chanu.

161 Zindikirani kulakwitsa kopupuluma bwanji wamalonda uyu-...Zomwe a—anali wamalonda wosauka bwanji, kuti anayesetsa kugwiritsitsa ku mwambo, pamene izo zinatsimikiziridwa kwa iye ndi kutsimikiziridwa kuti Apa panali Moyo Wamuyaya, ndipo iye anachitira umboni mofanana pa kumufunsa Yesu za izo.

162 Paulo anavomereza izo. Ife tikudziwa momwe iye anatulukira. Monga anthu a tsikuli, iwo amakonda lingaliro lotchuka, ndi mayamiko a munthu mmalo mwa ulemu wa Mulungu. Paulo sankasamala za matamando a munthu. Iye ankafuna ulemu wa Mulungu.

163 Tiyeni timutsatire mnyamata wamng'ono uyu mphindi chabe ife tisanatseke. Tiyeni timutsatire iye. Ife tikupeza malo otsatira, kuti, mnyamata uyu, inu mukudziwa zimene zinamuchitikira iye? Iye sanakhale wopemphetsa, chifukwa chochita izi. Iye sanadzakhale wopemphetsa mu msewu. Iye anawonjezekera mu katundu. Iye anali atawukana mwayi.

164 Nthawi zambiri, anthu lero amaseka ndi kuwuseleula Mzimu Woyera, ndiye nkumapitirira ndi kumatukuka mmalonda awo. Inu mukudziwa, mundikhululukire kuyankhula uku...Koma pamene iwo akuseka, ndikuti, "Bwanji, taonani, ine! Ngati pali chirichonse kwa Iwo, mwaona, bwanji, izo zikanachitika kwa ine, chinachake chikanachitika kwa ine."

165 Inu mukudziwa, pali a—a—mwambi, wakuti, "Zitsiru zimayenda ndi nsapato zagogoda pamene Angelo amawopa kupondapo."

166 Mnyamata mwini chuma uyu anachita zimenezo. Mukuona? Iye anapanga a—kulakwitsa kowopsya, ndipo ife tikupeza kuti izo sizinatchinge konse malonda ake. Iye analemera. Iye anakhala wotchuka kwambiri, anapeza katundu wochuluka. Ife tikupeza kuti, patapita kanthawi, kuti iye anafika pokula kwambiri mpaka ngakhale iye anachita kumanga nkhokwe zatsopano kuti ayikemo zinthu zake.

167 Ndipo chifukwa chakuti mpingo wakana Mzimu Woyera, mmasiku otsiriza ano, iwo wachulukidwa. Ndipo tsopano inu mukupita mu Ecumenical Council, ndendende basi chimene Baibulo linati inu mukanadzachita. Tsopano ndinu Laodikaya kwenikweni, "wolemera ndi wochulukidwa mu katundu," chimodzimodzi basi monga mnyamata ameneyo anachitira.

168 Iye anali choimira cha mpingo, kukana. Paulo anali choimira cha mmodzi wolandirayo. Awiri onse a iwo anali nawo mwayi, monga inu muli nawo usikuuno, ndipo ine ndiri nawo.

169 Iye anawonjezekera mu katundu. Momwemonso mpingo, M'badwo wa Laodikaya, wachulukidwa mu katundu. Ndipo kumbukirani, iye anakhala wamkulu kwambiri, mpaka iye anadzakhala wotchuka kwambiri, mpaka ngakhale mafumu, anthu opambana, anayamba kumabwera. Ndipo anapanga phwando lalikulu, nthawi ina.

170 Ndipo panali wogwirizira ndondomeko ya Moyo Wamuyaya pamalo ake ogulitsira, ndipo ife tikupeza kuti iye anali atagona pansi pakhomo. Oh, iye amakhoza kusesa zinyenyetswa zina zakugwa kuchokera kwa iye. Iye anali nawo mwayi apanso, mboni, Lazaro akumuchitira iye umboni. Koma iye amangosesa zinyenyetswazo, "Oh, chabwino, ine ndiyesetsa izi, nditenga gawo ili, kapena chirichonse," inu mukudziwa. Ndiko kachitidwe ka 1964. "Oh, ine ndithandizira pang'ono. Izo ziri bwino, ingomusiyani iye azipita, mwaona."

171 Koma iye anagwiritsitsa ndondomekoyo. "Osauka mu mzimu," Mateyu 5 amatiuza ife kuti ndi ameneyo, "wawo ndi Ufumu wa Kumwamba."

172 Iye amachulukirachulukira mu katundu, ndipo amapambanirapambanira ndi kutchuka kwambiri, ndipo munthu wamkulu, koma kulipiridwa kwake potsiriza kunadzabwera. Iko potsiriza kunadzabwera. Pa dziko lapansi iye anali ndi kulipiridwa kwakukulu. Iye anali ndi mwambo waukulu wa maliro, sindikukaikira. Mlaliki wamkulu wa chipembedzo anabwera, mwinamwake anayankhula mawu aakulu pa iye. Iwo mwinamwake anatsitsa mwatheka mbendera. Amuna amalonda abwino anamunyamulira iye kupita ku manda ake. Koma Baibulo linati, "mu gehena," malipiro ake anabwera chifukwa chokana ndondomeko ya Moyo Wamuyaya.

173 "Mu gehena iye anakwezera maso ake mmwamba, pakuti anali mu kuzunzika." Ndipo anayang'ana kutali

kudutsa phompho lalikulu, limene Yesu anati palibe munthu anayamba waolokapo kapena adzatero, ndipo iye anakamupeza wogwirizira ndondomeko ya Moyo Wamuyaya, akutonthozedwa, kumbali inayo. Awiri onse a iwo. Mmodzi anali atawulandira Iwo. Awiri onsewo anali ndi kulipiridwa kwawo. Wosesa-zinyenyetswa anali ndi malipiro ake. Ndipo tsopano wolemerayo anadzakhala wopemphetsa, "Mumulole wogwirizira ndondomekoyo abwerere ndipo adzakhudze milomo yanga ndi—madzi pang'ono, pakuti malawi awa akundizunza ine."

174 Musati mudzapange kulakwitsa komweko, munthu wamalonda. Ndinu wachivundi chimodzimodzi monga iwo anali. Inu muyenera mupange chigamulo. Mupange kulowetsako chuma kwanu tsopano. Mupange izo motsimikizika. "Mupange chisankho chanu, kuyitana motsimikizika." Mutulutse imodzi ya ndondomekozo.

175 Muyang'ane basi—mphindi chabe kapena ziwiri zowonjezera, ngati inu mungathe. Pamene Mose, amene anasiya, pokhala mfumu ya Igupto, Farao, kuchiwerengera chitonzo cha Khristu. Farao ankayang'ana pa anthu amenewo ngati gulu la oponda matope, koma Mose ankayang'ana pa iwo ngati anthu a lonjezo.

Kodi inu mumayang'ana motani pa iwo, anthu a Mulungu?

176 Mose anali ndi kulipiridwa kwake. Penyani onyamula maliro ake. Baibulo linati iwo anali "Angelo." Chifukwa chiyani? Panalibe aliyense akanakhoza kukamutengera iye kumene iye anali kupita. Iwo anali onyamula maliro ake.

177 Panali Eliya mu nthawi imene akazi onse ankadula tsitsi lawo, monga Akazi a Kennedy ndi iwo akuchitira lero. Amapenta nkhope zawo, Yezebeli. Mfumu ndi anthu onse ankapita mwachidziko; mpingo unkachita, nawonso. Ndipo Mulungu anatumizako mneneri, dzina lake Eliya, kuti akatsutse chinthu chimenecho. Iye atakalamba ndipo atatopa, iye anali wokonzeka kuti azipita Kwawo, iye sankasowa ngakhale kuti afe. Malipiro ake anabwera, nayenso, Mulungu anangomutumizira iye pansi gareta ndi akavalo ena, ndipo anamunyamulira iye mpaka Mmiyamba.

178 Stefano, yemwe anaima pa Sanhedrin, anayankhula kwa iwo ndipo anati, "Oh, inu owumamakosi, osadulidwa mu mtima ndi mmakutu, kukana ndondomeko, inu nthawizonse mumawukaniza Mzimu Woyera. Monga makolo anu anachitira, chomwechonso inu mukutero." Pa imfa yake, iye anali ndi kulipiridwa. Iye anayang'ana mmwamba ndipo anawona Miyamba itatseguka, Yesu atayima padzanja lamanja.

179 Moody, masiku otsiriza, pafupifupi zaka handiredi zapitazo, wosoka nsapato wamng'ono wa ku Chicago, samatha nkomwe kulemba dzina lake. Nyuzipepala inatumizidwa

kuti akamufunse Moody, nthawi ina. Utumiki wake unali wopambana kwambiri, iwo ankafuna kuti amuwone iye akuyika mu pepala chimene chinapangitsa izo; chimene chinali chokhudza Moody, ndi mlaliki wa mtundu wanji yemwe iye ayenera kukhala ali, ndi mlaliki wamphamvu. Kotero iwo anaitanitsa kuyankhulana kwapadera, kuti akalembe mu mkonzi wawo. Ndipo Moody sanakhoze ngakhale kuziwerenga izo iwo atatha kulemba izo, kotero manenjala wake ankayenera kuti amuwerengere iye zimenezo. Ndipo iye anati . . .

180 Apa ndi momwe za mkonzi zikuwerengekera. Iwo anati, "Chifukwa chimene aliyense amapitira kukamumvera Dwight Moody akulalikira, sindingathe kuzifotokoza izo." Anati, "Chinthu choyamba, iye ndi munthu wosawoneka bwino yemwe ine ndinayamba ndamuwonapo, wadazi ndi ndevu zikulendewera pansi." Ndipo anati, "Iye ali monga—iye ndi wamkulu monga iye ali wamtali." Ndipo anati, "Pamene iye akuyesetsa kuti alalikire, iye samakhoza kuwerenga. Ndipo iye amalira pamene iye akulalikira, amayankhulira mmphuno zake, ndi kuyankhula mwalikhweru."

181 Pamene iye watsiriza, Bambo Moody amangogwedeza mapewa ake, ndipo anati, "Ndithudi ayi. Iwo amabwera kudzamuwona Khristu." Chotero izo zinali zimenezo. Ziribe kanthu kuti otsutsa anali chiyani, iye anali ndi ndondomeko.

182 Ndipo pamene iye anali kufa, ndipo adokotala anati, "Ndi imfa imene yakukanthani, Bambo Moody."

183 Iye anadzuka, iye anati, "Inu mukuitcha iyi imfa? Ili ndi tsiku langa lovekedwa korona." Mukuona? Iye anagwirizira ndondomeko.

184 Mzanga wabwino, Paul Rader. Pamene ine ndinali mnyamata wamng'ono, ine ndinali—ine ndinadzozedwa mu mpingo wa Missionary Baptist, ndipo Paulo Rader anali wa Missionary Baptist nayenso, chotero, Fort Wayne, pamene ine ndinkapita kukamumvera iye akulalikira. Kenako, anadzabwera kuno ku West Coast ndipo anadzakhala ndi mavuto ochuluka, ndi vuto la zachuma mpaka iye anadzadwala, potsiriza anadzakhala ndi khansa, ndipo anali akufa. Iye ndi Luke ankayendera limodzi moyo wawo wonse, anamamatirana limodzi monga mwana wanga ndi ine.

185 Kotero pamene Paulo anali kufa, Moody Bible Institute inatumiza oyimba anayi, ndipo iwo anali atayima pamenepo. Paulo anali ndi kuseketsa. Ndipo iye anali . . . Wamphamvu pang'ono . . . Moody Bible Institute yaing'ono, ndi kwayara iyi, anali ataitumiza kumusi kumeneko, kapena oyimba anayi, ndipo iwo anali akuyimba, *Pafupi, Mulungu Wanga, Kwa Inu.*

186 Paulo anatembenuka ndipo anaponyera nsalu pa iye. Iye anati, "Ndani akufa, ine kapena inu?" Mukuona? Iye anati, "Kwezera mmwamba makatani amenewo, ndipo

muzindiyimbira ine nyimbo zina zabwino za Uthenga.” Ndipo iwo anayamba kuyimba:

> Pansi pa mtanda pamene Mpulumutsi wanga
> anafera,
> Pansi apo ponditsuka ku tchimo ndinalira;
> Pomwe mtima wanga Magazi anapakidwa;
> Ulemelero kwa Dzina Lake!

187 Paulo anati, “Alikuti m’bale wanga, Luke?” Luke anali mchipinda chinacho. Iye sanafune kuti amuwone m’bale wake akufa. Anati, “Kamuwuzeni iye kuti abwere kuno.”

188 Chotero Luke analowa mmenemo. Ambiri a inu mumamudziwa iye, munthu wamkulu wojintcha. Iye anadzalowa mkati. Paulo anafikira dzanja lake, atagona pa kama, ndipo anamutenga Luke pa dzanja ndipo anayang’ana mmwamba mu nkhope yake, anati, “Luke, ife tabwera mtunda wautali limodzi. Koma taganiza za zimenezo, Luke; mu maminiti faivi kuchokera pano ine ndidzakhala nditaima mu Kukhalapo kwa Yesu Khristu, nditavekedwa mu chirungamo Chake.” Atagwirizira manja a m’bale wake, ndondomeko yake inalipira.

189 Dokotala Bosworth wokalamba, yemwe anali kuno nthawi yotsiriza, ndi ine, pafupi ndi nthawi yotsiriza, usinkhu wa zaka eyite-foro, ndikungobwera kuchokera ku Afrika. Ine ndinali ndi kuitana “bwerani ku Miami.” Ine ndinang’amba matayara a galimoto yanga, pafupifupi, kuti ndikafike kumeneko. Anati, “Iye anali akufa.” Ine ndinathamangira kwa iye. Ine ndinkadziwa kuti iye anali atagwirizira ndondomeko. Ine ndinapita kumeneko.

190 Ine ndinapita mchipinda uko. Mnyamata wamng’ono wa mutu wa dazi ali ndi mikono yake mmwamba, mikono yake yaing’ono yowonda. Ine ndinathamangira kwa iye ndipo ndinakagwera pa nkhope yanga, ndipo ndinalira, “Atate anga, atate anga, magareta a Israeli ndi amuna apa kavalo ake!” Anaika manja ake pa ine ndipo anandidalitsa ine.

Ine ndinati, “M’bale Bosworth, kodi ine ndingakupempherereni inu?”

Anati, “Ayi.” Anati, “Ine sindikudwala.”

Ine ndinati, “Chavuta ndi chiyani, M’bale Bosworth?”

Anati, “Ine ndikungopita Kwathu.”

191 Ine ndinati, “Ine ndimadziwa zimenezo.” Ndipo ndinati, “Ine ndikufuna ndikufunseni inu chinachake, M’bale Bosworth.” Ine ndinati, “Inali liti nthawi yopambana ya moyo wanu ndi utumiki wanu? Inu mwakhala mukumutumikira Mulungu ine ndisanabadwe. Ife takhala tiri ku minda ya umishoni limodzi. Ife takhala tiri mmikuntho, mu mlengalenga ndi pa nyanja. Inu mumayima pafupi ndi ine pamene ine ndimawona ziwanda kumbali zonse, ndi asing’anga. Ndipo zimakhala zokondoweza

kwambiri pamene ife timamuwona Mulungu akuzifotetsa zimenezo apo. Chinali chiyani chokondoweza chachikulu cha moyo wanu?"

192 Iye anati, "Pakali pano." Iye anali akukonzekera kuti alipiridwe ndondomeko yake. Iye anati, "Zonse zimene ine ndazikhalira moyo, M'bale Branham, wakhala ali Yesu Khristu, ndipo miniti iliyonse Iye akubwera pakhomo kuti adzanditengere ine Kwathu."

193 Inde, amenewo anali ogwirizira ndondomeko omwe anapereka zonse zomwe anali nazo, ndi kukayika chuma chawo mu Ngale yamtengo wapatali. Kodi inu simukaika chuma chanu, usikuuno, nanunso, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu?

194 Ine sindikukhoza kuwona pa omvetsera onse. Ine sindikudziwa chimene. . .ndi angati, kapena amene akuyang'ana mkati, mu televizioni yotsekeredwa usikuuno. Ine ndikufunsa iwe, mzanga, usalole awa akhale mawu opanda pake. Ndiwe wachivundi. Iwe uyenera kufa. Iwe ukudziwa zimenezo. Ndipo izo zikhoza kukhala usanafike mmawa nthawi yako idzabwera. Ine sindiri. . . si munthu wokonda zokakamiza; ndipo, chifukwa Yesu anati, "Onse amene Atate andipatsa Ine adzadza." Ngati pali malo mu mtima a ndondomeko imeneyo, usikuuno, kodi inu simuwavomereza Iwo? Ndondomeko imeneyo ndi Khristu, ndondomeko ya chikondi cha Mulungu kwa inu, Mawu Ake kuti akhale amoyo mu mtima mwanu, kukupangani inu kukhala gawo la Iye. Iye ndi Mawu. Mulandireni Iye mmoyo wanu. Kodi inu simuchita zimenezo, ndi kupanga kulowetsako chuma kwakukulu uku?

195 Monga momwe ine ndingakhoze kuwonera, ine sindingakhoze kuwona koma pafupifupi mapazi teni kuchokera kwa ine, kapena fifitini. Ine ndikufunsani inu kuti mukweze mmwamba manja anu ngati inu mukufuna kuti mulandire imodzi ya ndondomeko za Moyo Wamuyaya. Munene kuti, "Ine ndikuifuna iyo, M'bale Branham. Mungondikumbukira ine mmapemphero anu. Inu simukuwona dzanja langa, koma Mulungu akutero."

196 Atate athu Akumwamba, iyi yophweka, yamwano, komabe nkhani yoona ya moyo. Ine ndinayankhula izi mwanjira iyi, Ambuye, chifukwa chakuti anthu, anthu amalonda, akanamvetsa izo mochuluka mwanjira ya kukhala chinachake choimiridwa kuno padziko lapansi. Ndi chifukwa chake ine ndimachitcha icho ndondomeko. Ndikhululukireni ine ngati ine ndinalakwitsa potchula zimenezo. Pakuti, ife tsopano tiri mu—mphindi yopatulika kwenikweni, pamene sindikukaika kuti alipo ambiri akuganiza motsimikiza tsopano, podziwa kuti iwo nawonso ayenera kulipira pa chirichonse chimene iwo ali

nacho pano, ndipo iwo akuwona chimene icho chimatanthauza kukana.

197 Tsopano, mnyamata ameneyo, monga ine ndikudziwira, mwinamwake pokhala wotchuka kwambiri pakati pa anthu, iye anatsalira mu tchalitchi, iye anasunga malamulo, iye sanachite chigololo, kapena kuba, kapena kuchita zinthu zimenezo, koma mu mtima wake womwe iye ankadziwa kuti iye analibe Moyo Wamuyaya. Muwathandize iwo, Ambuye, amene akuyesetsa kuti akumane ndi Inu, pofuna Moyo Wamuyaya, podalira makhalidwe abwino amenewo, mulole iwo usikuuno alandire kuitanako, ndipo angokhala pa mapazi awo, ndi kuti, "Ambuye, ine ndichita chirichonse chimene Inu mwandifunsa ine kuti ndichite." Perekani izi, Ambuye.

198 Iwo onse ndi Anu tsopano. Ine ndikupereka chirichonse kwa Inu. Ndipo ngati mbewu yagwera paliponse, Ambuye, pa nthaka iliyonse, mbewu iliyonse yokonzedweratu, kwa zaka zambiri yakhala ikuchita njala ndi ludzu, iyo ikhoza kugwera pa ena kwinakwake usikuuno. Mulole iwo alandire Moyo, Atate, pakuti ine ndikupempha izi mu Dzina la Yesu Khristu.

199 Ndipo ndi mitu yathu yoweramitsidwa mopitirira, ine ndimufunsa M'bale Pearry, ngati iye angathe, kuti abwere kuno ndi kudzatsalira, kudzapitiriza kotsalira kwa msonkhanowu.

64-0314 Kulowetsako Chuma
Beaumont Hotel
Beaumont, Texas U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org